

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

MALANGIZO NDI CHILIMBIKITSO KUCHOKERA M'BAIBULO
KUPITA KWA AMENE AKULALIKIRA UTHENGA WABWINO

TAONA, NDIDZA MSANGA

“Pakuti sitinatsata miyambi yachabe, pamene tinakudziwitsani mphamvu ndi maonekedwe a Ambuye wathu Yesu Khristu... Ndipo tili nao mau a chinenero okhazikika koposa; amene muchita bwino powasamalira...” (2 Petro 1:16, 19).

Chikhulupiriro ndiponso moyo wa mkhristu sizikhazikika pa nthano kapena nkambakamwa chabe, koma zaima pa kukwaniritsidwa kwenikweni kwa mauneneri osiyanasiyana. Izi zinachitika kwa nthawi yokwanira pafupifupi zaka 2,000. Aneneri akale lomwe analosera momveka bwino za kubadwa, moyo, imfa ndi kuukanso kwa Mesiya, Yesu Khristu. Zinthuzi sizidangochitika mwangozi kapena mwa nzeru za munthu. Koma zinthu zimene Baibulo linalosera zinachitika monga momwe zidanenedwera. Baibulo ndi losiyana ndi mabuku ena amene analembedwa, chifukwa ndi loona, lokhulupirika komanso lamphamvu ndipo limagwira ntchito.

Pali maulosi ena okhudzana ndi kutha kwa dziko amene sanakwaniritsidwe mpaka pano. Podziwa kuti Baibulo ndi

lodalirika, nanga ndani angakane zinthu zimene zikubwera kutsogoloko? Nthawi zowawitsa zili pa dzikoli. Ulosi womaliza mwa maulosi ukukwaniritsidwa.



*“Musachedwe, koma
konzekeretsani mtima wanu
ku moyo wosatha.”*

Dzikoli likunka liyipirayipira mu uchimo ndipo zizindikiro za nthawi zikuonetsa kuti dzikoli silitenga nthawi. Ano ndi

masiku otsiriza enieni a masiku otsiriza. Yesu akubweranso kachiwiri kuti adzatenge mtundu wa anthu ku chiweruzo kumene munthu aliyense adzaweruzidwa molingana ndi ntchito zake (Mateyu 16:27). Monga m'mene mauneneri olosera za kubwera koyamba kwa Yesu anakwaniritsidwa, chomwechonso mauneneri olosera za kubweranso kwake kwachiwiri adzakwaniritsidwa.

Anthu akukhala ngati kuti moyo udingopitirira basi. Iwo akufulatira Mulungu ndipo akukhala moyo wauchimo ndi wosaopa kapena kulabadira za moyo wosatha. Yesu akubweranso ngati “mbala panthawi ya usiku” (2 Petro 3:10). Pamene anthu asakuyembekeza, pamenepo dziko lidzatha ndipo onse adzafika ndi kuimirira pa mpando wakuweruza wa Mulungu kuti akalandire mphotho yamuyaya kapena chilango chamuyaya (2 Akorinto 5:10). Mulungu mu kuleza mtima kwake, wachedwetsa chiweruzo

(Yapitirira pa tsamba 2)

Mau a Mkonzi

Tsamba 3

Kusanthula Baibulo-
Za masiku omaliza

Tsamba 4

Za Nthawi yomaliza

Tsamba 5

Mafunso ndi Mayankho:
Kodi kudzakhalala ula-
muliro wa zaka 1,000

Tsamba 7

Kodi Mukudziwa?

Mau a pa Nyengo yake

Tsamba 8

zimene BAIBULO limaphunzitsa za...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;

Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chihero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;

Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;

Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;

1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chihero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;

1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;

Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

chake popeza Iye “safuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa” (2 Petro 3:9).

Pamene Yesu anakwera kunka kumwamba ataukitsidwa, mngelo wa Ambuye analankhula ndi ophunzira kuti: “Yesu amene walandiridwa kunka Kumwamba kuchokera kwa inu, adzadza momwemo monga munamuona alinkupita Kumwamba” (Machitidwe 1:11).

Yesu akubweranso. Pamene adzabwera, sipadzakhala nthawi yoti nkulapa, kapena nthawi yoti nkupemphera, kapenanso nthawi yoti nkusintha. Mudzafika ndi kuimirira pamaso pa Mulungu monga m'mene mulirimo.

“Taonani, ndidza msanga; ndipo mphotho yanga ndili nayo yakupatsa yense monga mwa ntchito yake” (Chivumbulutso 22:12). Kodi mukumva mau a Khristu? “ONANI NDIDZA MSANGA.” Nthawi yatsala yochepa mu dziko lino la uchimo. Ndondomeko ya ziweruzo za Mulungu pa munthu zimene zinachitika kale ikuonetsa kuti dzikoli likuyendera nthawi yobwerekaka. Nthawi ndi yochepa. Palibe chitsimikizo chakuti mawa lifika. Kodi mwakonzeka kukumana ndi Mulungu?

Yesu akubweranso ndipo ndi posachedwapa. Musachedwe, koma konzekeretsani mtima wanu ku moyo wosatha. (2 Akorinto 6:2). Ngati simunapululumutsidwe, lapani tchimo lanu panopa nthawi ndi mwayi zikanalipo ndipo mupulumutsidwe ndi mwazi wa Yesu Khristu.

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa mkalata umene umasindikizidwa m'dzina la Ambuye kwa anthu onse ku maiko onse ndi cholinga chofuna kuwakhazikitsa ndi kuwalimbikitsa mu choonadi cha Mau a Mulungu. Kalata yu akuphunzitsa ndi kulimbikitsa zoonadi za Baibulo zimene zakhazikitsidwa kuyambira pa nthawi ya Khristu ndi ya atumwi.

Mau a Mulungu ndi okhawo amene ali muyeso wowomerezeka wa chikhulupiriro. Amaphunzitsa chipulumutso ndi mamasulidwe kuchokera ku uchimo kudza mu ntchito ya maombedwe ya mwa Yesu Khristu; komanso kudzazidwa ndi Mzimu Woyera kumene kumatsatirapo. Ndipo kumatithandiza kuti titsogolere, tiwongolere ndi kuwapatsa ena mphamvu; komanso tikhale ndi chihero choonekera pa gawo lililonse la moyo wa munthu kuphatikizapo mgwirizano ndi umodzi wa anthu a Mulungu. Utumiki wowomerezeka wa kwa Mulungu uli mu mwa anthu amene ubale wao wachikondi wazikika pa choonadi.

Akonzi: Michael & Rene Smith

KUTI MULANDIRE NAWO KALATAYI

Uthenga Wabwino wa Choonadi ndi uthenga wa kalata umene timasindikiza miyezi itatu iliyonse molingana ndi chitsogozo cha Ambuye. Kuti mulandire nawo kalatayi mwaulere pa *email*, pitani pa intaneti ndipo mutipeza pa www.thegospeltruth.us. Muli omasuka kutitumizira maina ndi ma *email* a anthu amene akufuna kulandira nawo kalatayi. Mainawa muwatumize kwa mkonzi.

KUTI MUTIPEZE

Uthenga Wabwino wa Choonadi imasindikizidwa mu maiko osiyanasiyana kuti igawidwe m'maikowo. Ntchito yosindikiza kalatayi komanso mautumiki ena ochitika ndi ofesi yathu pothandiza kufalitsa uthenga wabwino amathandizidwa ndi zopereka zaufulu zoperekedwa mdzina la mpingo wa Mulungu.

Mau a Mkonzi



“Ndidza msanga; gwira chimene uli nacho, kuti wina angalande korona wako” (Chivumbulutso 3:11).

Kwa miyezi ingapo ndithu, ndakhala ndikutsimikizika mkati mwa mtima wanga kuti nthawi yathu yokhala padziko lino lapansi yatsala pang’ono kutha. Sindikukhulupirira kuti Ambuye achedwetsa kubweranso kwake. Uthenga uwu wa kubweranso kwake ukunditakasa mkati mwangamu.

Ndikukumbutsidwa za mneneri, Yesu mwana wa Ananiya, amene anayenda m’miseu ya ku Yeusalemu namalirira mzindawo chifukwa cha chionongeko chimene chinali pafupi. Iye anati, “Tsoka, tsoka kwa Yerusalemu.” Anthu amanena kuti wazungulira mutu ndipo anayesera kuti amukhalitse chete. Mzindawo umaoneka kuti unali pa mtendere ndipo unali kuchita bwino zedi. Komabe iye anapitirira kulira kuti, “Tsoka, tsoka – liwu lochokera kum’mawa, liwu lochokera ku madzulo, liwu lochokera ku mphepo zonse zinayi, liwu lotsutsa Yerusalemu...” Iye ananenera kwa zaka zisanu ndi ziwiri komanso miyezi isanu. Uneneriwa unakwaniritsidwa ndipo Yerusalemu anaonongeka.

Anthu akhoza kuwunyoza ndi kutopa nawo uthengawu, koma ine ndili wokonzeka kukhala ngati Ananiya. Nthawi yatsala pang’ono. Ambuye abweranso posakhalitsa. Mugwiritsitse chimenechi ndipo mukhale oonadi. Mukhale tsiku lililonse ngati ndi tsiku lanu lomaliza, popeza posachedwapa lidzakhaladi lomaliza. Dziko lapansi likunka liyipirayipira ndipo machitachita a Satana akuonekera kwakukulu pakati pathu. Mphamvu ikadalipo kuti munthu akhoza kukhala moyo wopatulika ndi wachiyero kudzera mwa Yesu Khristu, koma tikuyenera kukhala pafupi ndi mtanda.

Mu uthenga wathu wa mu Gospel Truth ulendo uno, tikhala tikukambana za mutu wa kubweranso kwa Khristu komanso za masiku omaliza. Pali kusamvetsetsa kwakukulu komanso ziphunzitso zabodza pa mutu umenewu. Tiyenera tiyang’ane Mau a Mulungu ndi kuwasanthula moonadi. Choonadi ndicho chida chenicheni chimene tingagwiritse ntchito polimbana ndi chinyengo. Mutu tikukambiranawu ndi waukulu ndipo sitingathe kupeza malo okwanira kuti ndithe kutambasula mokwanira bwino malemba onse amene akunena za mutuwu. Mwatsokanso, panalibenso malo okwanira polemba za mauneneri ena a mu buku la Chivumbulutso ndipo izi zabweretsa chisokonezo pa chiphunzitso cha “Masiku Omaliza”. Pamene tikuphunzira Mau a Mulungu, poyamba ndikofunika kutenga izo zimene zili zachidule ndi zosavuta kuzitsatira kenaka nkuzigwiritsa ntchito ngati kalozera pofuna kumvetsetsa ma uneneri ovutirapo komanso kuyankhula kwa zifanifani kumene timakupeza m’buku la Chivumbulutso.

Pali zinthu zina zazing’onozing’ono zopezeka m’Baibulo zimene Mulungu sadatiwululire, koma anati-patsa malangizo okwanira kuti tikathe kukalowa kumwamba. Miyandamiyanda ya anthu imapusitsidwa ndi chiyembekezo chabodza chakuti kudzakhalala ufumu wina kutsogoloko. Kenaka zimenezi zimawapangitsa iwo kuti asawafunefune Ambuye ndi mtima wao onse pamene ali m’moyo uno.

Chonde pitirizani kupemphera kuti Ambuye atsogolere ndi kudalitsa ntchito imene tikugwira ndi utumiki umenewu wa Gospel Truth komanso Africa Mission & Beyond. Tsiku ndi tsiku timadalira kuti Mzimu wa Ambuye atisogolere ndi kutipatsa zimene tikufuna pa utumiki umenewu umene uli Wake.

Nthawi yatha, Yesu akubwera posachedwapa.

Michael W. Smith

July 2013



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.us

kuti mudzilandira

makalata athu kapenanso

kuti muone makalata

akale.



KUSIYIDWA?

Chiphunzitso cha mkwatulo chasesa dziko lonse lino monga muja uma-chitira moto wamtchire.

Mau akuti, 'mkwatulo' amatanthauza 'kukumana ndi amene anatsogola' kapenanso 'kutengedwa'. Ziphunzitso zambiri za chikhristu zimaphunzitsa kuti olungama adzatengedwa ndi Ambuye kupita kumwamba pamene osalungama 'adzasiyidwa' pansi pano pamene padzakhale nthawi ya mazunzo.

Malemba amene amagwiritsidwa ntchito amachokera ku 1 Atesalonika 4:16-17 amene akuti, "Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba ... ndipo akufa mwa Khristu adzayamba kuuka; pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga..."

Paulo amalemba olungama pamene amawauza kuti, "tonthozanani ndi mau awa." Iye samakamba za matsiriziro a iwo osadziwa Mulungu. Yesu anati, "onse ali m'manda adzamva mau ake, nadzatulukira..." (Yohane 5:28-29).

Padzakhala chiukitso chimodzi cha dziko lonse lapansi ndi chiweruzo chimodzi cha dziko lonse. Palibe amene adzasiyidwe, popeza tonsefe tidzaima pamaso pa mpando wakuweruza wa Mulungu.

KALAZERA POSANTHULA MAU A MULUNGU

MUTU: ZA MASIKU OTSIRIZA - *Ziphunzitso za Mau a Mulungu zokhudzana ndi masiku omaliza*

Mau a Mulungu:

Yakobo 5:8 Lezani mtima inunso, limbitsani mitima yanu; pakuti kudza kwake kwa Ambuye kuyandikira.

Kuomba mkota: Yesu Khristu adzabweranso kachiwiri padziko lino lapansi pamene padzakhalsano chiukitso cha akufa onse ndipo anthu onse adzatengedwa kupita ku mpando wakuweruza wa Mulungu. Dziko lino lidzaonongedwa ndipo olungama adzakhala ndi moyo kumwamba mpaka muyaya ndipo osalungama adzakhala ku gehena.

I. Kubweranso Kachiwiri kwa Khristu

- A. Yohane 14:28 Yesu adzabweranso.
- B. Machitidwe 1:9-11 Adzaonekera.
- C. I Atesalonika 5:2 Monga mbala.
- D. Mark 13:32 Nthawi yosadziwika.
- E. Luka 12:40 Mosadziwika.
- F. Chivumbulutsa 1:7 Diso lililonse lidzamuona.
- G. I Atesalonika 4:16 Ndi mfuu waukulu.

II. Chiukitso chimodzi cha dziko lonse

- A. Yohane 5:28-29 Cha onse amene ali m'manda.
- B. Machitidwe 24:15 Cha onse olungama ndi ochimwa.
- C. I Atesalonika 4:16-18 Olungama poyambirira.
- D. I Akorinto 15:51-53 Adzaukitsidwa ndi thupi losaonongeka.

III. Chionongeko cha dziko lino

- A. 2 Petro 3:7-12 Dziko lino lidzapsa.
- B. Mateyu 24:35 Lidzapita ndithu.
- C. Ahebri 1:10-11 Lidzaonongeka.

IV. Chiweruzo

- A. 2 Akorinto 5:10 Onse adzaweruzidwa.
- B. Yohane 12:48 Adzaweruzidwa pa tsiku lomaliza.

C. Machitidwe 17:31 Dziko lidzaweruzidwa ndi Khristu.

D. 2 Timoteo 4:1 Amoyo ndi akufa adzaweruzidwa.

E. Aroma 14:10-12 Aliyense adziwunike.

F. Mlaliki 12:14 Zinsinsi zidzaweruzidwa.

V. Za Chiweruzo (Chiweruzo, Mphotho ndi Chilango)

- A. Mateyu 25:31-46
- B. Chivumbulutsa 20:11-15
- C. Chilango chosiyanasiyana
- D. Aroma 2:6 Monga mwa ntchito zao.
- E. Luka 12:47-48 Pali kusiyana kwa chilango.
- F. Onaninsu: 2 Petro 2:21; Ahebri 10:29.

VI. Chilango Chosatha – Gehena

- A. Onani Za chiweruzo
- B. Masalmo 9:17 Gehena.
- C. 2 Petro 2:9 Chilango.
- D. 2 Atesalonika 1:9 Kwamuyaya.
- E. Mateyu 24:50-51 Kulira.
- F. Chivumbulutsa 21:8 Moto ndi miyala yonyeka.
- G. Luka 16:23-26 Chizunzo cha gehena.

VII. Mphotho Yosatha – Kumwamba

- A. Onani Za Chiweruzo: Moyo wosatha.
- B. I Petro 1:4-5 Cholandira chathu kumwamba.
- C. 2 Akorinto 5:1 Chopangidwa chopanda manja.
- D. Ahebri 11:16 Dziko lakumwamba.
- E. Chivumbulutsa 7:15-17 Kulibe njala kapena misozi.
- F. Chivumbulutsa 21 ndi 22 Kutofokozera za Kumwamba.

Mau Omaliza

Chivumbulutsa 22:20 Iye wakuchitira umboni izi, anena, Indetu; ndidza msanga. Amen; idzani, Ambuye Yesu.

ZA NTHAWI YOMALIZA

Tsatanetsane wa mau othandizira pa kusanthula kwa Mau Mulungu

MAU A MULUNGU NDIYE KALOZERA WATHU

Kubweranso kachiwiri kwa Khristu komanso zinthu zina zimene zidzatsatirepo zili zofunikira kwambiri. Pali malemba ochuluka ndi mauneneri ambiri okhudza za masiku omaliza. D.S. Warner ananena kuti, “Zimene anthu anakhazikitsa ndi zongopeka siziphula kanthu pamene tikunena za zinthu zimene zidzachitike mtsogolo.” Pamene tikufuna kumvetsetsa za mutuwu, ndikofunikira kwambiri kuti malemba adzitisogolera koposa nzeru ndi ukachenjede wa anthu. Malemba amalozera ku nthawi ya mtsogolo pamene Yesu adzabwerenso. Kudzakhala chiukitso cha anthu onse akufa, chiweruzo cha anthu onse, kulandira mphotho yosatha ndi kulandira chilango chosatha ndipo dziko lapansili lidzaonongedwa.

YESU ADZABWERANSO

Yesu anawauza ophunzira ake kuti, “Ndidzabweranso.” (Yohane 14:3,28). Mngelo wa Ambuye anatsimikiza za choonadi chimenechi pamene Yesu amakwera kunka Kumwamba ataukitsidwa (Machitidwe 1:11). Yesu adzabweranso monga imachitira mbala nthawi ya usiku (1 Atesalonika 5:2) pamene anthu sakumuyembekezera. Ambiri otchedwa aneneri akhala akuyesera kupereka tsiku lenileni limene Ambuye adzabwere, “Koma za tsiku ilo, kapena nthawi yake sadziwa munthu, angakhale angelo m'Mwamba, angakhale Mwana, koma Atate ndiye” (Marko 13:32). Ndi chifukwa chake, munthu aliyense ayenera kukhala maso ndi kukhala wokonzeka. “...chifukwa nthawi imene simulingirira, Mwana wa Munthu akudza.” (Luka 12:40).

NTHAWI IDZAFIKA KUMAPETO

Tsiku limene Yesu adzabwerenso kudzamaliza zinthu zonse pansi pano lidzakhala tsiku la ulemerero ndi loopsa. Olungama adzasangalala ndipo osalungama adzalilira kuti miyala yaikulu ndi mapiri ziwagwere. Yesu adzabwera m'mitambo ndipo

“diso lililonse lidzampenya lye” (Chivumbulutso 1:7). “Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mfuu, ndi mau a mngelo wamkulu, ndi lipenga la Mulungu...” (1 Atesalonika 4:16). Iye adzabwera “mu ulemerero wa Atate wake, pamodzi ndi angelo ake” (Mateyu 16:27).

AKUFA ADZAUKA

Pamene Yesu adzabweranso m'mitambo, padzakhala chiukitso cha anthu onse. “m'kamphindi, m'kuthwanima kwa diso, pa lipenga lotsiriza; pakuti lipenga lidzalira, ndipo akufa adzaukitsidwa osavunda, ndipo ife tidzasandulika.” (1 Akorinto 15:52). Pamene ambiri amaphunzitsa kuti olungama okha ndiwo adzaukitsidwa, Malemba amaphunzitsa kuti, “kudzakhala kuuka kwa olungama ndi osalungama” (Machitidwe 24:15). “Musazizwe ndi ichi, kuti ikudza nthawi, imene onse ali m'manda adzamva mau ake, nadzatulukira, amene adachita zabwino, kukuuka kwa moyo; koma amene adachita zoipa kukuuka kwa kuweruza” (Yohane 5:28-29).

DZIKO LAPANSILI LIDZAONONGEDWA

Mau a Mulungu amanena mvemvemve kuti dziko lapansili lidzaonongedwa (Mateyu 24:35; Ahebri 1:10-11). “koma miyamba ndi dziko la masiku ano, ndi mau omwewo zaikika kumoto, zosungika kufikira tsiku la chiweruzo ndi chionongeko cha anthu osapembedza” (2 Petro 3:7).


Pamene Yesu adzabweranso kudzayamba kuweruza mtundu wa anthu, kumwamba timakuonaku ndi dziko lapansili zidzatha ndipo zidzaotchedwa. Dzikoli

lidzaonongedwa ndipo zake zonse zidasungunuka ndi moto wootcha kwambiri (2 Petro 3:10-12).

ALIYENSE ADZAIMA PAMASO PA MULUNGU

Pa tsiku lalikulu limenelo limene lili tsiku lomaliza, pa tsiku la Ambuye, Khristu adzaweruza dziko lapansi. Iye “adzaweruza

(Yapitirira pa tsamba 6)



CHIWERUZO

*“Pakuti kwalembedwa,
Pali moyo wanga, ati Ambuye,
mabondo onse adzagwadira Ine,
ndipo malilime onse
adzavomereza Mulungu.”*

Aroma 14:11

(Kuchokera pa tsamba 5)

amoyo ndi akufa, ndi pa maonekedwe ake” (2 Timoteo 4:1). Anthu onse a mbadwo uliwonse, a mtundu uliwonse, ndi chinenero chilichonse, ndi fuko lililonse adzaimirira pamaso pa mpando wakuweruza wa Khristu. Munthu aliyense wa chikhulupiriro chilichonse ndi chipembedzo chilichonse adzapinda bondo ndi kuvomereza kuti Yesu ndiye Ambuye (Aroma 14:1-12). Zidzakhala zonyaditsa komanso zoopsa pa chiweruzo chimenechi pamene aliyense adzapereke kwa Mulungu ntchito zimene anachita. Zinsinsi zonse zidzaululika ndipo palibe chimene chidzabisika (Mlaliki 12:14).

PADZAKHALA CHIWERUZO CHIMODZI CHOMALIZA

Pa Mateyu 25:31-46 ndi pa Chivumbulutso 20:11-15 akutionetsa za m'mene chiweruzo chidzayendere. “ndipo adzasonkhanidwa pamaso pake anthu a mitundu yonse; ndipo lye adzalekanitsa iwo wina ndi mnzake” (Mateyu 25:32). Pamene anthu onse adzaimirira pamaso pa Mulungu, buku la moyo lidzatsekulidwa (Chivumbulutso 20:12) ndipo munthu aliyense adzaweruzidwa ndi Mau a Mulungu (Yohane 12:48) ndipo adzalandira mphotho kapena chilango “monga momwe anachita, kapena chabwino kapena choipa” (2 Akorinto 5:10).

KUDZAKHALA KUSIYANA KWA CHILANGO

Mphotho yamuyaya ndi chilango chamuyaya zidzaperekedwa pa chiweruzo chomaliza. Kumalo kumene tikakhale kwamuyaya zitengera zisankho zimene tingachite pa moyo uno. “Taonani, ndidza msanga; ndipo mphotho yanga *ndili* nayo yakupatsa yense monga mwa ntchito yake” (Chivumbulutso 22:12). Mulungu adzapereka chiweruzo chachilungamo ndipo “adzabwezera munthu aliyense kolingana ndi ntchito zake” (Aroma 2:6). Ngati munthu amvetsetsa bwino za Mulungu ndi choonadi, ameneyo akafunsidwa zambiri ndipo akalangidwa ngati atakana choonadicho. “Ndipo kapolo uyo, wodziwa chifuniro cha mbuye wake, ndipo *sanakonza*, ndi kusachita zonga za chifuniro

chakecho, adzakwapulidwa *mikwapulo* yambiri. Koma iye amene sanachidziwe, ndipo anazichita zoyenera mikwapulo, *adzakwapulidwa* pang'ono” (Luka 12:47-48). (Onaninso 2 Petro 2:21, Ahebri 10:26-29, Mateyu 11:20-24).

OSALUNGAMA ADZAPITA KU GEHENA KU CHIZUNZO CHOSATHA

Mulungu wasungira “osalungama kufikira tsiku loweruza akalangidwe” (2 Petro 2:9). Chilango cha oipa chidzakhala ku gehena (Masalimo 9:17). Gehena ndi malo amene anthu adzakhala mpaka muyaya, ndipo kuli chionogeko chamuyaya (2

Atesalonika 1:9). Mu buku la Chivumbulutso 21:8 likunenedwa monga ngati “nyanja yotentha ndi moto ndi sulufure”. Pa chiweruzo, Yesu adzanena kwa ochimwa kuti, “Chokani kwa Ine otembereredwa inu, kumoto wa nthawi zonse wokolezedwera mdierekezi ndi angelo ake” (Mateyu 25:41). Ndi malo amene kudzakhala “kulira ndi kukukuta mano” (Mateyu 24:51). Popeza chabwino chilichonse sichidzakhala, amene adzakhale kumeneko sadzatha

kuuthawa ululu wosatha, mavuto osatha, kukumbukira kosatha ndi mdima wosatha.

OPULUMUTSIDWA ADZALOWA KUMWAMBA KUCHISANGALALO CHOSATHA

Pamene anthu osalungama adzatengedwa kupita ku chilango chosatha, olungama adzalandira moyo wosatha ngati cholowa chao (Mateyu 25:45-46). Popeza kuli “cholowa chosavunda ndi chosadetsa ndi chosafota, chosungikira m'Mwamba” (1 Petro 1:4). Mulungu wakonzeratu mzinda wakumwamba (Ahebri 11:6) kumene mau athu sangathe kufotokoza mokwanira bwino maonekedwe ake (2 Akorinto 12:4). Ndi mzinda wokongola mochititsa kaso ndipo uli ndi zonse zimene zili zabwino ndi zokoma pofuna kupereka mphoto kwa olungama. (Onani Chivumbulutso 21 ndi 22).

-mws



Mafunso ndi Mayankho

Funso: Kodi kudzakhala ulamuliro wa zaka 1,000?

Yankho: Funso limeneli ndi lofunikira popeza kwachuluka kusamvetesetsa komanso chiphunzitso chabodza zokhudzana ndi kubweranso kwa Khristu. Yankho lake ndi 'ayi'.

SIPADZAKHALA ULAMULIRO WA ZAKA 1,000.

Pamene mipingo ili ndi zikhulupiriro zosiyanasiyana pa mutuwa, ganizo lakuti kudzakhala ulamuliro wa zaka 1,000 limaphatikizapo chiphunzitso chakuti Khristu adzabweranso ku dziko lapansi ndi kudzakhazikitsa 'Ufumu wake kwa zaka 1,000'. Iwo amakhulupirira kuti Yesu adzakhazikitsa likulu la ufumu wake ku Yerusalemu ndipo adzalamulira pa maiko onse a dziko lapansi kwa zaka 1,000 chisanafike chiweruzo chomaliza. Izi zikusiyana ndi chiphunzitso chomveka bwino cha Mau a Mulungu pa mutu wa kubweranso kwa Khristu ndi chikhalidwe cha Ufumu wa Mulungu.

SIPADZAFUNIKIRA ZAKA 1,000 popeza kuti Khristu adzakhala atakhazikitsa kale Ufumu wake. Yesu pa Yohane 18:36 adati, "Ufumu wanga sulika ku dziko lino lapansi; ufumu wanga ukadakhala wa dziko lino lapansi, anyamata anga akadalimbika nkondo..." Pamene Afarisi anamulamulira Yesu kuti awauze kuti Ufumu wa Mulungu udzafika liti, Yesu adawayankha powauza kuti, "Ufumu wa Mulungu sukudza ndi maonekedwe; ndipo sadzanena, Taonani uwu, kapena uwo! Pakuti, taonani, Ufumu wa Mulungu

uli m'kati mwa inu" (Luka 17:20-21). Ufumu wa Mulungu ndi ufumu wa uzi-mu. "Pakuti ufumu wa Mulungu sukhalachakudya ndi chakumwa, koma chilungamo, ndi mtendere, ndi chimwemwe mwa Mzimu Woyera" (Aroma 14:17). Ufumu wa Khristu wa padziko lino lapansi unakhazikitsidwa m'mitima mwa okhulupirira pamene iye anabwera panthawi yoyamba. Anthu a Mulungu akulamulira tsopano (Aroma 5:17). Ntchito ya Khristu pa dziko pano inamalizika pamene anabwera panthawi yoyamba ija. "Ine ndalemekeza Inu pa dziko lapansi, m'mene ndinatsiriza ntchito imene munandipatsa ndichite" (Yohane 17:4).

***"Molingana ndi Malemba,
Sipadzafunikira zaka 1,000,
Sipadzakhala nthawi ya zaka 1,000,***



***Sipadzakhala malo
a zaka 1,000."***

Iwo amene amagwiritsitsa maganizo amenewa akuti kudzakhala ulamuliro wa zaka 1,000 amapusitsika poyang'ana Khristu atakhala pampando wachifumu wa Davide m'masiku am'tsogolo. Koma zoonza zake ndi zakuti mpando waufumu wa Davide unathetsedwa kalekale. Mpando wa ufumu wa Davide umaimira mphamvu ndi ufumu zaulemelero. Yesu anabadwa monga "mfumu ya Ayuda" (Mateyu 2:2). Pamene Herode analowa mu Yerusalemu, khwimba la anthu linaimba mofuula kuti, "Ndipo akutsogolera, ndi iwo akutsata, ana-

fuula, Hosana; Wolemekezeka Iye wakudza m'dzina la Ambuye: Wolemekezeka Ufumu ulinkudza, wa atate wathu Davide; Hosana m'Kumwambamwamba" (Marko 11:9-10).

SIPADZAKHALA ULAMULIRO WA ZAKA 1,000 pamene Khristu adzabweranso. Kudzakhala chiukitso chimodzi cha akufa (Yohane 5:28-29) patsiku lomaliza (onani Yohane 6:39-40, 44, 54). Sikudzakhala chiukitso chosiyana cha anthu olungama ndi anthu osalungama. Khristu adzaweruza anthu onse pamodzi (Mateyu 25:31-34, 41, 46) pamene adzalandire mphoto zamuyaya. Zonsezi zidzachitika 'patsiku lomaliza'.

SIPADZAKHALA MALO A ULAMULIRO WA ZAKA 1,000

Pamene Khristu adzaonekera. Talingalirani ndime iyi yopezeka pa 2 Petro 3:7,10. "koma miyamba ndi dziko la masiku ano, ndi mau omwewo zaikika kumoto, zosungika kufikira tsiku la chiweruzo ndi chionongeko cha anthu osapembedza. ... Koma tsiku la Ambuye lidzadza ngati mbala; m'mene miyamba idzapita ndi chibumoso chachikulu, ndi zam'mwamba zidzakanganuka ndi kuthatha kwakukulu, ndipo dziko ndi ntchito zili momwemo zidzatenthedwa." Malemba akuchitira umboni mwachimvekere kuti pamene Yesu adzabweranso, dzikoli lidzaonongedwa kotheratu ndi moto. Izi zidzachitika pa tsiku la chiweruzo pamene Ambuye adzabweranso ngati m'mene imachitira mbala pa nthawi ya usiku.

Molingana ndi Malemba, sipadzafunikira zaka 1,000, sipadzakhala nthawi ya zaka 1,000, ndipo sipadzakhala malo a ulamuliro wa zaka 1,000. Chiphunzitso cha zaka 1,000 ndi chinyengo cha mdani. Anthu ambiri akufunafuna ndi kuyembekezera mwai wina m'masiku alinkudza. Palibenso mwai wachiwiri, popeza lero ndi tsiku la chipulumutso. Ino ndiyo nthawi tsopano yolowa mu Ufumu wa Mulungu ndi kukonzekera nthawi yamuyaya.


-mws



KODI MUKUDZIWA

Malemba: Machitidwe 2:27 Pakuti simudzasiya moyo wanga kudziko la akufa, kapena simudzapereka Woyera wanu aone chivunde. (Malemba ena ofanana nao: Masalmo 16:10)

Dziko la Akufa ndi mau ochokera ku Chigriki akuti 'Hades' ndiponso ku Chihebri 'Sheol'. Amene amatanthauza: *manda, chikhalidwe cha anthu akufa, malo a mizimu yakufa.*



Pamene Yesu anafa pamtanda sanapite ku malo a anthu akufa kwa Satana. Mizimu wake unakwera kupita ku Paradiso, - malo a chisangalalo ndi chimwemwe.

Yesu anamuza wachifwamba uja pa mtanda paja kuti, "Lero, udzakhala ndi ine mu Paradaiso" (Luka 23:43).



Mau a pa Nyengo Yake

Lowani mu Chikondwerero cha Mbuye Wanu

KUTI MUTIPEZE

The Gospel Truth
605 Bishops Ct.
Nixa, MO 65714
USA
Email:
editor@thegospeltruth.us

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Mateyu 25:23 *Mbuye wake anati kwa iye, Chabwino, kapolo iwe wabwino ndi wokhulupirika; unali wokhulupirika pa zinthu zazing'ono, ndidzakhazika iwe pa zinthu zambiri; lowa iwe m'chikondwerero cha mbuye wako.*

Mau okoma kunenedwa kwa kapolo wa Mulungu wokhulupirika pamene waima pa mpan-do wakuweruza wa Mulungu. "Lowa iwe m'chikondwerero cha mbuye wako." Mavuto onse, kuwawa konse, kukhumud-witsidwa konse, kuda nkawa konse ndi mayesero onse a moyo uno zidzaoneka ngati zopanda ntchito pamene ti-dzalowa m'malo okongola kwambiri otchedwa 'Kumwamba', kumene Mulungu wakonzera anthu ake.



Chiyembekezo chokalowa Kumwamba chimanka chikuli-rakulira kwa mwana wa Mulungu. Likubwera tsiku limene sikudzakhalanso imfa, chisoni, misozi, matenda, kulumala, mayesero, ndi mavuto. Likubwera tsiku limene kudzakhala ulemerero, kukongola ndi chimwemwe pamaso pa Mfu-mu ya Mafumu ndi Mbuye wa Ambuye.

Sikudzafunikanso kuti dzuwa liwale ayi, popeza mwanawankhosa adzakhala kuwala kwake. Ulemerero ndi kuwala kwake zidzaposa zimene munthu akhoza kuganizira ndiponso thupi lathuli likhoza kuzilandira. Nchifukwa chake, atumiki a Mulungu adzakhale ndi thupi la ule-merero pa tsiku lalikulu la chiukitso limeneli kuti adzakhoze kulandira chidzalo cha ulemer-ero wamuyaya wa Kumwamba.

Khalani wokhulupirika ndi wosasunthika, inu kapolo wa Mulungu. Kumwamba kudzakhala kokoma zedi. Sizochesha ayi.

-mws